

KALATA YA PAULO YOLEMBERA FILEMONI

¹ Kuchokera kwa Paulo, amene ndili m'ndende chifukwa cha Khristu Yesu ndi Timoteyo m'bale wathu.

Kulembera Filemoni, bwenzi lathu lokond-edwa ndi mtumiki mnzathu.

² Kwa Apiya mlongo wathu, Arkipo msilikali mnzathu, ndiponso mpingo umene umasonkhana m'nyumba mwanu.

³ Chisomo ndi mtendere zochokera kwa Mulungu Atate athu ndi Ambuye Yesu Khristu zikhale ndi inu.

Kuyamika ndi Pemphero

⁴ Ine ndimayamika Mulungu wanga nthawi zonse ndikakukumbukira iwe m'mapemphero anga.

⁵ Pakuti ndamva za chikondi chako, za chikhulupiriro chako mwa Ambuye Yesu ndiponso za chikondi chako pa oyera mtima onse.

⁶ Ine ndikupemphera kuti mgwirizano wako ndi ife m'chikhulupiriro ukhale opindulitsa pozamitsa nzeru zako zozindikira zinthu zilizonse zabwino zimene timagawana chifukwa cha Khristu.

⁷ M'bale, chikondi chako chandipatsa chimwemwe chachikulu ndi chilimbikitso, chifukwa umatsitsimutsa mitima ya anthu a Ambuye.

Paulo Apempha kuti Amuchitire Chifundo Onesimo

⁸ Tsopano ngakhale kuti mwa Khristu nditha kulimba mtima ndi kulamulira kuti uchite zimene uyenera kuchita,

⁹ komabe ndikupempha mwachikondi. Ine Paulo, munthu wokalamba, ndipo tsopano ndili m'ndende chifukwa cha Khristu Yesu,

¹⁰ ndikukupempha chifukwa cha mwana wanga Onesimo, amene ndamubala ndili mu unyolo.

¹¹ Anali wopanda phindu kwa iwe, koma tsopano wasanduka wa phindu kwa iwe ndi kwa inenso.

¹² Ine ndikumutumizanso kwa iwe tsopano, koma potero ndikukhala ngati ndikutumiza mtima wanga weniweni.

¹³ Ndikanakonda ndikanakhala naye kuno kuti iyeyo azinditumikira m'malo mwako pamene ndili mu unyolo chifukwa cha Uthenga Wabwino.

¹⁴ Koma sindikufuna kuchita kanthu osakufunsa, n'cholinga chakuti chilichonse chabwino ungandichitire chikhale mwakufuna kwako osati mokakamiza.

¹⁵ Mwina chifukwa chimene unasiyana naye kwa kanthawi ndi chakuti ukhale nayenso nthawi zonse.

¹⁶ Osati ngati kapolo, koma woposa kapolo, ngati m'bale wokondedwa. Iyeyu ndi wokondedwa kwambiri kwa ine koma kwa iweyo ndi wokondedwa koposa, ngati munthu komanso ngati m'bale mwa Ambuye.

17 Tsono ngati umati ndine mnzako, umulandire iyeyu monga momwe ukanandilendirira ineyo.

18 Ngati anakulakwira kapena kukongola kanthu kalikonse, ndidzalipira ineyo.

19 Ine, Paulo ndikulemba zimenezi ndi dzanja langa. Ine ndidzalipira. N'kosafunika kukukumbutsa kuti iweyo ngongole yako kwa ine ndi moyo wakowo.

20 M'bale, ndikufuna kuti ndipindule nawe mwa Ambuye; tsono tsitsimutsa mtima wanga mwa Khristu.

21 Ine ndili ndi chitsimikizo cha kumvera kwako pamene ndikukulembera kalatayi. Ndikulemba ndikudziwa kuti udzachita ngakhale kuposa zimene ndakupemphazi.

22 Chinthu chinanso ndi ichi: undikonzere malo, chifukwa ndikukhulupirira kuti Mulungu adzamvera mapemphero anu ndi kundibwezera kwa inu.

Mawu Otsiriza

23 Epafra, wam'ndende mnzanga chifukwa cha Khristu Yesu akupereka moni.

24 Atumiki anzanga awa, Marko, Aristariko, Dema ndi Luka, akuperekanso moni.

25 Chisomo cha Ambuye Yesu Khristu chikhale ndi mzimu wako.

**Biblica® Tsekulani Mawu a Mulungu mu
Chichewa Chalero**
**Chichewa: Biblica® Tsekulani Mawu a Mulungu mu
Chichewa Chalero (Bible) of Malawi**

copyright © 2016 Biblica, Inc.

Language: Chichewa

Contributor: Biblica, Inc.

Biblica® Open God’s Word in Contemporary Chichewa™

Copyright © 2002, 2016 by Biblica, Inc.

“Biblica” is a trademark registered in the United States Patent and Trademark Office by Biblica, Inc. Used with permission.

Used with permission. All rights reserved worldwide.

All content on open.bible is made available under a Creative Commons Attribution-ShareAlike 4.0 License (<http://creativecommons.org/licenses/by-sa/4.0/>).

You are free to:

- Share — copy and redistribute the material in any medium or format
- Adapt — remix, transform, and build upon the material for any purpose, even commercially

Under the following conditions:

Attribution — You must attribute the work as follows: “Original work available for free at www.biblica.com and open.bible” Attribution statements in derivative works should not in any way suggest that we endorse you or your use of this work.

ShareAlike — If you remix, transform, or build upon the material, you must distribute your contributions under the same license as the original.

Use of trademarks: Biblica® is a trademark registered in the United States Patent and Trademark Office by Biblica, Inc. and may not be included on any derivative works. Unaltered content from open.bible must include the Biblica® trademark when distributed to others. If you alter the content in any way, you must remove the Biblica® trademark before distributing your work.

This translation is made available to you under the terms of the Creative Commons Attribution Share-Alike license 4.0.

You have permission to share and redistribute this Bible translation in any format and to make reasonable revisions and adaptations of this

translation, provided that:

You include the above copyright and source information.

If you make any changes to the text, you must indicate that you did so in a way that makes it clear that the original licensor is not necessarily endorsing your changes.

If you redistribute this text, you must distribute your contributions under the same license as the original.

Pictures included with Scriptures and other documents on this site are licensed just for use with those Scriptures and documents. For other uses, please contact the respective copyright owners.

Note that in addition to the rules above, revising and adapting God's Word involves a great responsibility to be true to God's Word. See Revelation 22:18-19.

2021-11-15

PDF generated using Haiola and XeLaTeX on 18 Apr 2025 from source files dated 16 Nov 2021

f540eb34-4377-5601-9dcf-0a053d172faa